# BWAILA CLUSTER TERM ONE EXAMINATIONS

## 2022-2023 JUNIOR CERTIFICATE OF EDUCATION

# CHICHEWA

**Subject Number: J032/II**

**Monday, 12th December 2022** **Time Allowed: 1h 45 min**

**08:00AM – 09:45AM**

## PEPALA LACHIWIRI

(Malikisi 50)

**Malangizo**

1. **Onesetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi atatu.**
2. Pepalali lili ndi magawo atatu **(A, B ndi C).** Yankhani **mafunso onse** m'magawo onse atatu**.**
3. Lembani **dzina lanu** pamwamba pa masamba **onse**.
4. Muchitebulo chili pambalichi, onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.
5. Perekani pepalali kwa oyang'anira mayeso nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| | | | |

## Gawo A: (Malikisi 20)

## KUMVETSA NKHANI

**1. Werengani nkhani ili m'munsiyi mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.**

Padali munthu wina yemwe adali ndi mdzukulu wake wokondana naye chifukwa ndiye adamutcha dzina. Atakula mwanayo adamutumiza kusukulu kukaphunzira kuti adzakhale mnyamata wokhala naye. Mwanayo adakonda sukulu mpaka adamaliza sukulu yake ataphunzira zaka khumi. Mnyamata adaganiza ntchito yofuna kuchita ndipo pomaliza adaganiza zopita kusukulu kuti akaphunzire ntchito yomanga nyumba ndi ntchito yopala matabwa. Adapitadi kusukulu kuja kumene adakhalako zaka ziwiri nabwerera kwawo kukayamba ntchito yake ya iye mwini.

Sadayambe ntchito yolembedwa ndi aliyense koma ntchito yake idali yopita uku ndi uku kukamanga nyumba za anthu omwe amafuna kuwamangira nyumba zawo.

Adali munthu wopata ndalama mwezi ndi mwezi koma adali kukhala ndi ngongole zambiri kwa anthu ena ndi ena ngakhale ndi kumasitolo komwe. Adalemba anthu omulimira minda yake koma osawalipira msanga. Pamene adaona kuti adali ndi ngongole zotere, samaoneka panyumba masana koma usiku wokha basi. Ndipo pochoka panyumba kupita ku ntchito, adali kuchoka mammawa okhaokha dzuwa lisadatuluke. Ngakhale amamanga nyumba za eni zokongola, koma nyumba ya iye mwini idali yamaonekedwe osakondweretsa, ndiponso pa nthawi ya mvula, sadathe kuona pamalo othawirapo chifukwa cha kudontha kwa nyumbayo. Banja lake lidali losakondwa kwenikweni chifukwa cha moyo umenewu wokhala osauka pamene sadayenera kukhala osauka.

Pamudzipaja padali munthu wina amene ankagwira ntchito ku dziko la ku Unangu. Iye atafika m'mudzimo adafuna kumangitsa nyumba yake kuti pomaliza ntchito yake pa zaka zowerengeka adzakhalemo. Ndipo adaona kuti woyenera kumanga nyumba yakeyo adali yemwe uja amene adali kumanga nyumba m'mudzimo ngakhale adali wangongole ndi anthu ambiri. Adapangana za nyumbayo nanena kuti potha nyumba yaikulu yonseyo adzalandira ndalama zokwanira K 1, 000, 000. Wofuna nyumba uja adabwerera kuntchito kwake.

Womanga uja adayamba kumanga nyumba ija, koma zilingo zake zomangira zidali zija zomwe zidali zopanda pake ndiponso zosalimba. Mwina mwambiri adamangira ndi mapesi a mapira. Adagwira ntchito mwaulesi koma adangofuna kudzalandira ndalama mosavuta, ndiponso monyenya. Potha nyumba ija idali yopotoka mbali imodzi mwakuti siikadakhala, ngakhale chaka chimodzi.

Mwini nyumba uja adabwera kuwona nyumba yake, mpaka adaona kuti siidali yokondweretsa monga mowe adaganizira, koma yoipadi. Adamuuza womanga uja nati, "Achimwene nyumbayi ndi yoipa imene ine sindingalowemo. Tsopano tengani nyumbayi ikhale yanu ndalama simulandira.'' Adali wachisoni kwambiri womangayo chifukwa chachimenechi ndikusakhulupirika kwake.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa**

a. Ndi ntchito yanji yomwe mnyamata yemwe akukambidwa m'nkhaniyi adasankha kuphunzira atamaliza sukulu?

________________________________________________________________________

________________________________________________________________(Malikisi 2)

b. Kodi mnyamatayu adatenga nthawi yaitali bwanji pofuna kuphunzira ntchitoyi?

________________________________________________________________(Malikisi 1)

c. Kodi mnyamatayu akalemba anthu omulimira m'munda amakhala nawo bwanji?

________________________________________________________________________

________________________________________________________________(Malikisi 2)

d. N'chifukwa chiyani mnyamatayu adali ndi mavuto pomwe ankapata ndalama mwezi ndi mwezi.

________________________________________________________________________

________________________________________________________________ (Malikisi 2)

e. Chimamuchititsa n'chiyani mnyamatayu kuchoka pa nyumba mammawa dzuwa lisadatuluke?

________________________________________________________________________

________________________________________________________________ (Malikisi 2)

f. Ndi chinyengo chanji chomwe adachita munthu yemwe adafuna kuti amumangire nyumba wa ku Unangu?

________________________________________________________________________

________________________________________________________________________

________________________________________________________________ (Malikisi 2)

g. Mchifukwa chiyani mwini nyumba uja sadafune kulowa mnyumba yatsopanoyi? Perekani zifukwa ziwiri.

________________________________________________________________________

________________________________________________________________(Malikisi 2)

h. Tsimikizani kuti mnyamata yemwe ankagwira ntchito ku dziko la ku Unangu adali wanzeru.

______________________________________________________________________________

______________________________________________________________________________

______________________________________________________________________________(Malikisi 2)

i. Perekani mawu ofanana m'matanthauzo ndo otsatirawa omwe atengedwa mnkhaniyi.

a) Ngongole: ______________________________________________

b) Osakondweretsa: ______________________________________________

c) Kusakhulupilika:______________________________________________

(Malikisi 3)

j. Perekani mawu mnkhaniyi omwe ndi otsutsana m'matanthauzo ndi awa:

a) Yoongoka: ______________________________________________

b) Mpondamatiki: ______________________________________________

(Malikisi 2)

**Gawo B: (Malikisi 20)**

**2. Werengani nkhani ili m'munsiyi mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.**

M'dera la Mfumu Chibisa munafika mzungu amene anamanga nyumba zogonamo ndi nyumba zogwiriramo ntchito anthu ake. Pamalo pamene anamanga nyumbazo anthu ankangopatchula kuti pa Boma.

Tsono popeza kuti azungu ndi anthu ochenjera kwambiri, kunapezeka kuti mzunguyo anakhazikitsa ulamuliro wake. Iye anayamba kulamulira anthu am'deralo ndipo anayamba kuwakhometsa anthuwo msonkho. Olephera kukhoma msonkho anali kumangidwa.

Komabe Boma linkamulipira *nswahala* Mfumu Chibisa mwezi uliwonse. Poona zimenezi, Mfumu Chibisa inkakhala mokondwa ndipo inkavomereza zilizonse zimene boma linkafuna.

Tsiku lina kunali msonkhano pamudzi pa Mfumu Chibisa. Msonkhanowo unali wokambirana zamalimidwe amakono omwe Boma linkafuna kukhazikitsa. Anthu ena anayamba kukana mtundu waulimiwo koma Boma linalalata kwambiri kuti: "Inu ndinu anthu opusa kwambiri. Bwanji mukufuna kumalimbana ndi ine boma? Kodi simudziwa kuti popanda ine palibe dziko?"

Bambo Mvano adadzuka mokwiya kwambiri ndipo anati: "Bwana, mukunenazo nzopanda mutu. Izi zikuonetseratu kuti mutu wanu suyenda bwino"

Bwana Boma anapsa mtima ndipo anati: “Ine mutu wanga suyenda bwino?”

Mvano anati: “Inde, ndipo mutuwo ndiwouma kwambiri. Inu simungaone nokha kuti muli pano ngati munthu waboma chifukwa chaife anthu tafika pano? Popanda ife inu simungakhale boma. Nchifukwa chake timati Boma ndi anthu osati inu.”

Bwana uja anakhala chete kumvetsera mwachidwi. Mvano anapitiriza kuyankhula.

“Ife ndi amene tikumanga Boma osati inuyo ayi. Taonani, inu pano mwachita msonkhano pakati pa anthu osati pakati pa mitengo kapena pakati panyama kapenanso nyumba zomwe munamanga. Nanga mwalekeranji kukachita msonkhano kuphiriko, kwa anyani? Mwabwera pano chifukwa cha ife anthu. Popanda ife anthu simungapange malamulo oti atsatidwe.”

Pamenepo mkulu wa Boma uja adati, “Mnyamatayu akufuna kudzetsa chisokonezo. Inu apolisi, mumangeni chifukwa afuna kuukira Boma.”

Mvano adati, “Inu mudamanga ndende komanso kulemba anthu ntchito yolondera akaidi chifukwa cha ife anthu wochimwa. Mutha kundimanga. Pakanapanda anthu ochimwa ngati ine, simukanamanga chinyumba chosungiramo akaidi ndipo apolisi anuwa sakanapeza ntchito.”

Pamenepo mkulu waboma uja anavomereza mwamanyazi m’mtima mawu a Mvano ndipo anaziyankhula motsitsa mawu kwambiri, “Ndi zoona zimene akunena mnyamatayu. Popanda anthuwa, ine sindingapeze ntchito ndiponso sindingapeze ulemu.”

Komabe posafuna kuonetsa kugonja, mkulu wa Boma uja anati, “Iwe mnyamata, ndachita nawe chisoni; usadzabwerezenso?”

Msonkhano unathera pompo popeza pamalopo panayamba kuchitika chipwirikiti.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa**

a. Kodi nkhaniyi ikuchitikira kuti?

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

b. Tchulani ampangankhani aakulu awiri munkhaniyi.

______________________________________________

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

c. Ndi chiyani chomwe chimachitika kwa omwe ankalephera kukhoma msonkho?

_______________________________________________

**(Malikisi 1)**

d. Perekani mfundo **imodzi** yosonyeza kuti ampangankhani ena anali olimba mtima munkhaniyi.

_______________________________________________

**(Malikisi 2)**

e. Kodi mawu okuti ***nswahala*** akutanthauzanji munkhaniyi?

_______________________________________________

**(Malikisi 1)**

f. Kodi nkhaniyi ili mu mphendero yanji?

_______________________________________________

**(Malikisi 1)**

g. Tsimikizani popereka mfundo **imodzi** kuti mzungu anali ndi moyo wosafuna kuonetsa kugonja.

_______________________________________________

**(Malikisi 2)**

**3.** Werengani ndakatulo ili m'munsiyi ndipo muyankhe mafunso otsatirawo

**Ndapita**

Mwana wanga
Ndatere panomu
Ndatsala amodzi okha
Ndingolindira tsikulo nkapume
Dzakumbuke abale ako
Thengo ndi mambala
Ukadzakhuphuka
Dzadziwe ndi m'mwamba
Chibale ndi fupa.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa**

a. Kodi akuyankhulayu chikumuchitikira n'chiyani?

_______________________________________________

**(Malikisi 2)**

b. Lembani kamvekedwe ka ndakatuloyi.

______________________________

**(Malikisi 2)**

c. Perekani chitsanzo **chimodzi** pa chipangizo chilichonse chomwe chili m'munsichi kuchokera m'ndakatuloyi.

i) Chining'a

______________________________

**(Malikisi 1)**

ii) Chiyerekezero

______________________________

**(Malikisi 1)**

d. Tchulani mfundo zikuluzikulu **ziwiri** zomwe zikupezeka m'ndakatuloyi.

i) ______________________________

______________________________

**(Malikisi 1)**

ii) ______________________________

______________________________

**(Malikisi 1)**

e. Perekani phunziro **limodzi** lomwe likupezeka m'ndakatuloyi.

______________________________

**(Malikisi 2)**

## Gawo C: (Malikisi 10)

**4. Masulirani kandime kali m'munsika m'Chichewa chomveka bwino.**

The natural disaster that affected the northern district of Karonga was probably the worst to hit Malawi. This natural disaster was an earthquake. The earthquake left so many people helpless.

______________________________

______________________________

______________________________

______________________________

______________________________

**(Malikisi 5)**

**5.** Fupikitsani kankhani kali m'munsika kuti kakhale ndi mawu osachepera **21** koma asapitilire **25**.

Achemwali ake a bambo ake amachita ulimi wachilimwe womwe amagwiritsa ntchito madzi a mu mtsinje. Achemwali awowa amapopa madzi mu mtsinjewu ndi makina wogwiritsa ntchito diziro ndipo amatsirira munda onse omwe uli kumtunda. Anthu ochokera kumzambwe, kumvuma, kumpoto ndi kummwera wa mudzi wawo amabwera kudzapikula lepu, mpiru, khwanya ndi kabitchi. Amayi amenewa amapeza phindu ndi kumaguliratu fetereza ndi mbewu.

______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________

**(Malikisi 5)**

# MAFUNSO ATHERA PANO

**NB: Pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi atatu**